

Woyera amanditsimikizira kuti ndine Mwana wa Mulungu. Choncho ndimamvera komanso kutsatira liwu la Yesu. Ndikachimwa, ndimalapa, ndikulandira chikhululukiro. Ndinabadwa mwatsopano, ndipo ndikukhala moyo watsopano, wachiyero.

Pomaliza, *“Yesani zonse, sungani chokomacho, mupewe maonekedwe onse achoipa. Ndipo Mulungu wa mtendere yekha ayeretse inu konse konse, ndipo mzimu wanu ndi moyo wanu ndi thupi lanu zisungidwe zamphumphu, zopanda chirema pakudza kwache kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.”* (1 Atesalonika 5:21-23).

Mulungu akudalitseni pamene mukuyenda naye.

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Written by: Mick Alexander
Email: leeandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz

Woyera amanditsimikizira kuti ndine Mwana wa Mulungu. Choncho ndimamvera komanso kutsatira liwu la Yesu. Ndikachimwa, ndimalapa, ndikulandira chikhululukiro. Ndinabadwa mwatsopano, ndipo ndikukhala moyo watsopano, wachiyero.

Pomaliza, *“Yesani zonse, sungani chokomacho, mupewe maonekedwe onse achoipa. Ndipo Mulungu wa mtendere yekha ayeretse inu konse konse, ndipo mzimu wanu ndi moyo wanu ndi thupi lanu zisungidwe zamphumphu, zopanda chirema pakudza kwache kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.”* (1 Atesalonika 5:21-23).

Mulungu akudalitseni pamene mukuyenda naye.

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Written by: Mick Alexander
Email: leeandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz

NJIRA YA MTENDERE

Kumva ndi kutsatira liwu la Ambuye

*“Nkhosa zanga zimva mawu
anga ndipo Ine ndizizindikira,
ndipo zinditsata Ine”.*
Yohane 10:27

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

NJIRA YA MTENDERE

Kumva ndi kutsatira liwu la Ambuye

*“Nkhosa zanga zimva mawu
anga ndipo Ine ndizizindikira,
ndipo zinditsata Ine”.*
Yohane 10:27

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Mu Buku Lopatulika, Mzimu Woyera
akutchulidwanso kuti:
Mzimu
Mzimu wa Yesu
Mzimu wa Khristu
Mzimu wa Yesu Khristu
Mzimu wa Atate
Mzimu wa Mulungu
Mulungu, Yesu ndi Mzimu Woyera ndi amodzi

Kumvera ndi kutsatira liwu la Yesu zitanthauzanso:
Kutsogozedwa ndi Mzimu
Kumvera Mzimu
Kukhala mwa Mzimu
Kuyenda mwa Mzimu
Kuyenda mwa chikhulupiriro
Kuyenda ndi Yesu
Kukhala mwa Yesu
Kukhalabe mwa Yesu

Kukhulupirira mwa Yesu kutanthauzanso:
Kuyenda ndi Yesu
Kuyenda ndi Ambuye
Kudalira mwa Yesu
Kupereka njira zako kwa Yesu
Kuika chikhulupiriro chako mwa Yesu
Kuyenda mwa chikhulupiriro
Kukhala moyo wa chikhulupiriro

Mu Buku Lopatulika, Mzimu Woyera
akutchulidwanso kuti:
Mzimu
Mzimu wa Yesu
Mzimu wa Khristu
Mzimu wa Yesu Khristu
Mzimu wa Atate
Mzimu wa Mulungu
Mulungu, Yesu ndi Mzimu Woyera ndi amodzi

Kumvera ndi kutsatira liwu la Yesu zitanthauzanso:
Kutsogozedwa ndi Mzimu
Kumvera Mzimu
Kukhala mwa Mzimu
Kuyenda mwa Mzimu
Kuyenda mwa chikhulupiriro
Kuyenda ndi Yesu
Kukhala mwa Yesu
Kukhalabe mwa Yesu

Kukhulupirira mwa Yesu kutanthauzanso:
Kuyenda ndi Yesu
Kuyenda ndi Ambuye
Kudalira mwa Yesu
Kupereka njira zako kwa Yesu
Kuika chikhulupiriro chako mwa Yesu
Kuyenda mwa chikhulupiriro
Kukhala moyo wa chikhulupiriro

pakuti popanda Ine simungathe kuchita kanthu. Ngati wina sakhala mwa Ine, watayika kunja monga nthambi, nafota, ndipo azisonkhanitsa nazitaya ku moto, nazitentha". Choncho tikuona kuti akhristu (nthambi) akuyenera kukhalabe mwa Yesu (Mpesa) apo ayi adzadulidwa nadzaponyedwa kumoto. (kukhalabe mwa Yesu kungotanthauza kupitilira kumvera komanso kutsatira liwu lake).

Chipulumutso chathu chikhoza kufanizidwa ndi nsomba. Pamene nsomba ikhalabe m'madzi, idzakhala ndi moyo, koma ikachoka m'madzi idzafa. Nsomba ikuyenera kukhalabe m'madzi kuti ikhale ndi moyo. Chimodzimodzi inu ndi ine, tikuyenera kukhalabe mwa Yesu kuti tikakhalebe opulumuka komanso kukakhala ndi Iye kwamuyaya. **1 Yohane 5:11c** akuti: "*Mulungu anatipatsa ife moyo wosatha ndipo moyo umene uli 'mwa' Mwana wake*".

Kabuku aka kanayamba ndikutifunsa kunso la m'mene tingamuyankhire munthu atatifunsa kuti tingadziwe bwanji kuti ndife opulumutsidwa. Yankho lake lingakhale motere: "Ndikudziwa kuti ndine wopulumutsidwa chifukwa Mzimu

pakuti popanda Ine simungathe kuchita kanthu. Ngati wina sakhala mwa Ine, watayika kunja monga nthambi, nafota, ndipo azisonkhanitsa nazitaya ku moto, nazitentha". Choncho tikuona kuti akhristu (nthambi) akuyenera kukhalabe mwa Yesu (Mpesa) apo ayi adzadulidwa nadzaponyedwa kumoto. (kukhalabe mwa Yesu kungotanthauza kupitilira kumvera komanso kutsatira liwu lake).

Chipulumutso chathu chikhoza kufanizidwa ndi nsomba. Pamene nsomba ikhalabe m'madzi, idzakhala ndi moyo, koma ikachoka m'madzi idzafa. Nsomba ikuyenera kukhalabe m'madzi kuti ikhale ndi moyo. Chimodzimodzi inu ndi ine, tikuyenera kukhalabe mwa Yesu kuti tikakhalebe opulumuka komanso kukakhala ndi Iye kwamuyaya. **1 Yohane 5:11c** akuti: "*Mulungu anatipatsa ife moyo wosatha ndipo moyo umene uli 'mwa' Mwana wake*".

Kabuku aka kanayamba ndikutifunsa kunso la m'mene tingamuyankhire munthu atatifunsa kuti tingadziwe bwanji kuti ndife opulumutsidwa. Yankho lake lingakhale motere: "Ndikudziwa kuti ndine wopulumutsidwa chifukwa Mzimu

Mulungu akhoza kuletsa lilime lathu ... tikamulola. **Yakobo 1:19** akuti: “*Mudziwa abale anga okonedwa kuti munthu ali yense akhale wotchera khutu, wodekha polankhula, wodekha pakupsa mtima*”. Nthawi zambiri ndimalankhula zinthu ndisanaganize, ndipo ndimamufunsa Mulungu kuti andithandize, Iye amamanga lilime langa. Ndimamuuza Mulungu kuti: “*Muike mdindo pakamwa panga, Yehova, sungani pakhomo pa milomo yanga*” (**Masalimo 141:3**).

Ndibwerezanso kunena mfundo yofunika iyi:

Pamene tachimwa (kapena kusachita chifuniro chake), mtendere wathu ndi Mulungu umasowa.

Pamene talapa, mtendere wathu umabwerera Nthawi iri yonse tikasowa mtendere, pali vuto pakati pa ife ndi Mulungu.

POMALIZA

Ndimaliza ndi mavesi amene akutiuzwa kuti chipulumutso chathu chiri ‘mwa’ Yesu. Yesu akufanizira moyo wathu mwa Iye ndi nthambi mu mpesa. **Yohane 15:5-6** akuti: “*Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake, wakukhala mwa Ine ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri;*

Mulungu akhoza kuletsa lilime lathu ... tikamulola. **Yakobo 1:19** akuti: “*Mudziwa abale anga okonedwa kuti munthu ali yense akhale wotchera khutu, wodekha polankhula, wodekha pakupsa mtima*”. Nthawi zambiri ndimalankhula zinthu ndisanaganize, ndipo ndimamufunsa Mulungu kuti andithandize, Iye amamanga lilime langa. Ndimamuuza Mulungu kuti: “*Muike mdindo pakamwa panga, Yehova, sungani pakhomo pa milomo yanga*” (**Masalimo 141:3**).

Ndibwerezanso kunena mfundo yofunika iyi:

Pamene tachimwa (kapena kusachita chifuniro chake), mtendere wathu ndi Mulungu umasowa.

Pamene talapa, mtendere wathu umabwerera Nthawi iri yonse tikasowa mtendere, pali vuto pakati pa ife ndi Mulungu.

POMALIZA

Ndimaliza ndi mavesi amene akutiuzwa kuti chipulumutso chathu chiri ‘mwa’ Yesu. Yesu akufanizira moyo wathu mwa Iye ndi nthambi mu mpesa. **Yohane 15:5-6** akuti: “*Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake, wakukhala mwa Ine ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri;*

NJIRA YA MTENDERE Kumva ndi kutsatira liwu la Ambuye

LIWU LOYAMBA

Munthu atakufunsani, “Mukudziwa bwanji kuti ndinu opulumutsidwa?”, mungawayankhe bwanji?

Mungathe kunena kuti, “Ndimakhulupirira mwa Yesu” ... koma satana amakhulupiranso ndipo akupita ku Gehena.

Kapena mungathe kunena, “Ndimapita ku tchalitchi” ... koma angakhale galu akhoza kulowa mu tchalitchi.

Kapena mungathe kunena, “Banja langa lonse ndi a Khristu” ... koma chipulumutso ndi wekha, ndipo palibe angalowe ufumu wa Mulungu kugwiritsa ntchito chiphaso cha mzake. Kupulumutsidwa, wina aliyense akuyenera kukhala ndi ubwenzi wayekha ndi Yesu.

Nanga, tingakhale bwanji pa ubwenzi ndi Yesu komanso kukhala ndi chitsimikizo kuti ndife opulumutsidwa?

Choyamba, Mzimu Woyera amakhala mwa munthu *aliyense* amene walapa tchimo ndi kukhulupirira pa Yesu. **Machitidwe 2:38**

NJIRA YA MTENDERE Kumva ndi kutsatira liwu la Ambuye

LIWU LOYAMBA

Munthu atakufunsani, “Mukudziwa bwanji kuti ndinu opulumutsidwa?”, mungawayankhe bwanji?

Mungathe kunena kuti, “Ndimakhulupirira mwa Yesu” ... koma satana amakhulupiranso ndipo akupita ku Gehena.

Kapena mungathe kunena, “Ndimapita ku tchalitchi” ... koma angakhale galu akhoza kulowa mu tchalitchi.

Kapena mungathe kunena, “Banja langa lonse ndi a Khristu” ... koma chipulumutso ndi wekha, ndipo palibe angalowe ufumu wa Mulungu kugwiritsa ntchito chiphaso cha mzake. Kupulumutsidwa, wina aliyense akuyenera kukhala ndi ubwenzi wayekha ndi Yesu.

Nanga, tingakhale bwanji pa ubwenzi ndi Yesu komanso kukhala ndi chitsimikizo kuti ndife opulumutsidwa?

Choyamba, Mzimu Woyera amakhala mwa munthu *aliyense* amene walapa tchimo ndi kukhulupirira pa Yesu. **Machitidwe 2:38**

komanso **Aefeso 1:13** akuti pamene munthu walapa, ndi kukhulupirira pa Yesu, amapulumsidwa ndipo Mzimu Woyera nthawi yomweyo amakhala mwa iyeyo. Choncho, ngati mwalapa, ndi kukhulupirira pa Yesu, mutsimikizike kuti ndinu opulumutsidwa chifukwa “*Mzimu yekha achita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu*” (**Aroma 8:16**).

Tsopano, tiyeni tiwone m'mene Mzimu amachitira umboni (kulankhula) mwa ife. Pa **Yohane 10:27**, Yesu akuti, “*Nkhosa zanga zimva mawu anga ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine*”. Choncho ngati timvera ndi kutsata liwu la Yesu, tizadziwa kuti tiri m'modzi mwa nkhoa zake, kutanthauza kuti, tiri m'modzi mwa ana ake. Kumvera liwu la Yesu ndi chimodzimodzi kumvera Mzimu chifukwa Mzimu Woyera amatchedwanso Mzimu wa Yesu. Nanga, zikutanthauza chani kumvera ndikutsata Yesu?

KODI KUMVERA

KUMATANTHAUZA CHANI?

Zokhudza Mzimu Woyera, **Yohane 16:8** akuti, “*Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za*

komanso **Aefeso 1:13** akuti pamene munthu walapa, ndi kukhulupirira pa Yesu, amapulumsidwa ndipo Mzimu Woyera nthawi yomweyo amakhala mwa iyeyo. Choncho, ngati mwalapa, ndi kukhulupirira pa Yesu, mutsimikizike kuti ndinu opulumutsidwa chifukwa “*Mzimu yekha achita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu*” (**Aroma 8:16**).

Tsopano, tiyeni tiwone m'mene Mzimu amachitira umboni (kulankhula) mwa ife. Pa **Yohane 10:27**, Yesu akuti, “*Nkhosa zanga zimva mawu anga ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine*”. Choncho ngati timvera ndi kutsata liwu la Yesu, tizadziwa kuti tiri m'modzi mwa nkhoa zake, kutanthauza kuti, tiri m'modzi mwa ana ake. Kumvera liwu la Yesu ndi chimodzimodzi kumvera Mzimu chifukwa Mzimu Woyera amatchedwanso Mzimu wa Yesu. Nanga, zikutanthauza chani kumvera ndikutsata Yesu?

KODI KUMVERA

KUMATANTHAUZA CHANI?

Zokhudza Mzimu Woyera, **Yohane 16:8** akuti, “*Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za*

ku tchimo; TSATIRANI pakulapa.

MTENDERE NDICHOTITSOGOLERA

MU ZONSE

Takhala tikuyang'ana za tchimo, koma mtendere wa Mulungu niye chotitsogolera muzonse. **Afilipi 4:6-7** akuti “*Musadere nkhoa kose, komatu m'zonse ndi pemphero ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu*”. Choncho pamene tifunsa, Mulungu azatipatsa nzeru zoganiza, zolankhula komanso zochita, ndipo mudzakhala ndi mtendere pamene njira zanu zikhala mu chifuniro chake. Iye adzachotsa mtendere wanu pamene mulankhula, munganiza, komanso kuchita motsutsana ndi chifuniro chake. Pamene mupempherera kanthu kena, ndipo muli ndi mtendere mu mtima, pitirizani chifukwa Mulungu amalemekeza mapemphero athu ndipo amatipatsa mtendere pamene tichita zinthu molingana ndi chifuniro chake.

ku tchimo; TSATIRANI pakulapa.

MTENDERE NDICHOTITSOGOLERA

MU ZONSE

Takhala tikuyang'ana za tchimo, koma mtendere wa Mulungu niye chotitsogolera muzonse. **Afilipi 4:6-7** akuti “*Musadere nkhoa kose, komatu m'zonse ndi pemphero ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu*”. Choncho pamene tifunsa, Mulungu azatipatsa nzeru zoganiza, zolankhula komanso zochita, ndipo mudzakhala ndi mtendere pamene njira zanu zikhala mu chifuniro chake. Iye adzachotsa mtendere wanu pamene mulankhula, munganiza, komanso kuchita motsutsana ndi chifuniro chake. Pamene mupempherera kanthu kena, ndipo muli ndi mtendere mu mtima, pitirizani chifukwa Mulungu amalemekeza mapemphero athu ndipo amatipatsa mtendere pamene tichita zinthu molingana ndi chifuniro chake.

zake za thupi, mudzakhala ndi moyo. Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu”.

1 Yohane 3:6a komanso **3:10b** akuti: *“Yense wakukhala mwa Iye sachimwa ... Yense wosachita chilungamo siali wochokera kwa Mulungu, ndi iye wosakonda m’bale wake”.*

Akolose 1:21-23 akuti, *“Ndipo inu okhala alendo kale ndi adani m’chifuwa chanu m’ntchito zoipazo, koma tsopano anakuyanjanitsani m’thupi lake mwa imfayo, kukaimika inu woyera ndi opanda chirema ndi osatsutsika pamaso pake – ngatitu mukhalabe mchikhulupiro, ochirimika ndi okhazikika, ndi osasunthika kulekana nacho chiyembekezo cha uthenga wabwino”.*

Ma vesi amenewa, komanso mavesi ena ambiri, akuti uza kuti ngati tikana kutsutsa kwa Mzimu Woyera, ndikupitiriza kukhala moyo wa uchimo mwadala, tiri pa ngozi ya moto waku Gehena. Tiyeni tonse tiunikire **Yakobo 1:22** amene akuti: **“Khalani akuchita mawu, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha”.** Choncho musangomvere kokha pamene Mzimu akutsutsani

zake za thupi, mudzakhala ndi moyo. Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu”.

1 Yohane 3:6a komanso **3:10b** akuti: *“Yense wakukhala mwa Iye sachimwa ... Yense wosachita chilungamo siali wochokera kwa Mulungu, ndi iye wosakonda m’bale wake”.*

Akolose 1:21-23 akuti, *“Ndipo inu okhala alendo kale ndi adani m’chifuwa chanu m’ntchito zoipazo, koma tsopano anakuyanjanitsani m’thupi lake mwa imfayo, kukaimika inu woyera ndi opanda chirema ndi osatsutsika pamaso pake – ngatitu mukhalabe mchikhulupiro, ochirimika ndi okhazikika, ndi osasunthika kulekana nacho chiyembekezo cha uthenga wabwino”.*

Ma vesi amenewa, komanso mavesi ena ambiri, akuti uza kuti ngati tikana kutsutsa kwa Mzimu Woyera, ndikupitiriza kukhala moyo wa uchimo mwadala, tiri pa ngozi ya moto waku Gehena. Tiyeni tonse tiunikire **Yakobo 1:22** amene akuti: **“Khalani akuchita mawu, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha”.** Choncho musangomvere kokha pamene Mzimu akutsutsani

machimo, ndi zachilungamo, ndi zachiwerozo” choncho, pamene tichimwa, Mzimu amatitsutsa ndipo timasowa mtendere.

Pamene tinama, timasowa mtendere.

Pamene tiba, timasowa mtendere.

Pamene tida anzathu, timasowa mtendere.

Pamene tisilira, timasowa mtendere ndipo

Pamene tikhumba zonyasa, timasowa mtendere.

Pamene tasowa mtendere, china chake

chalakwika pakati pa inu ndi Mulungu, ndipo

muyenera kubwerera kwa Iye mu pemphero

ndikumufunsa chifukwa chani ndikusowa

mtendere – nthawi yomweyo Iye

adzakuyankhani. Izi ndiye tanthauzo la

kumvetsera. KUMVETSERA ndi kuzindikira

kuti mwasowa mtendere, ndikumufunsa Mulungu

chifukwa chani wakuchotserani mtendere.

KODI KUTSATIRA

KUMATANTHAUZA CHANI?

KUTSATIRA ndi kulapa tchimo lomwe Mulungu

(Mzimu) akukutsutsani nalo. Pamene mukufika

pamaso pa Mulungu ndi kulapa, mufike

ndimalingaliro owona. Kulapa sikunena kuti,

“Eya, Eya, ndikudziwa kuti ndachimwa koma

ndine wathupi la nyama” uku ndikufuna

machimo, ndi zachilungamo, ndi zachiwerozo” choncho, pamene tichimwa, Mzimu amatitsutsa ndipo timasowa mtendere.

Pamene tinama, timasowa mtendere.

Pamene tiba, timasowa mtendere.

Pamene tida anzathu, timasowa mtendere.

Pamene tisilira, timasowa mtendere ndipo

Pamene tikhumba zonyasa, timasowa mtendere.

Pamene tasowa mtendere, china chake

chalakwika pakati pa inu ndi Mulungu, ndipo

muyenera kubwerera kwa Iye mu pemphero

ndikumufunsa chifukwa chani ndikusowa

mtendere – nthawi yomweyo Iye

adzakuyankhani. Izi ndiye tanthauzo la

kumvetsera. KUMVETSERA ndi kuzindikira

kuti mwasowa mtendere, ndikumufunsa Mulungu

chifukwa chani wakuchotserani mtendere.

KODI KUTSATIRA

KUMATANTHAUZA CHANI?

KUTSATIRA ndi kulapa tchimo lomwe Mulungu

(Mzimu) akukutsutsani nalo. Pamene mukufika

pamaso pa Mulungu ndi kulapa, mufike

ndimalingaliro owona. Kulapa sikunena kuti,

“Eya, Eya, ndikudziwa kuti ndachimwa koma

ndine wathupi la nyama” uku ndikufuna

kupitiriza kuchimwa. Kulapa ndikubwera pamaso pa Mulungu ndi mtima wosweka ndikunena kuti, “Ambuye, ndachimwira inu. Ndikudziwa kuti ndikuyenera kupita ku Gehena. Chonde, mundikhululukire ndi kundiyeretsa ku tchimoli pakuti sindikufuna kupitilira kukhala mu uchimo”. Mukuyenera kukhala ndi malingariro owona pamene mukulapa. (2 Akorinto 7:10) Ngati mtima wanu siuli woongoka, simukhululukidwa komanso simupatsidwa mphamvu yokana tchimo. Pa Masalimo 51:17, Davide anaonetsa mtima owona ku tchimo lake pamene akunena kuti, “Nsembe za Mulungu ndizo mzimu wosweka, inu Mulungu, simudzaupeputsa mtima wosweka ndi wolapa”. Davide anasweka mtima ku tchimo lake, ifenso tikuyenera kutero popeza Mulungu amadana ndi tchimo.

Choncho, **KUMVETSERA** ndi kuzindikira kuti mwasowa mtendere, ndikumufunsa Mulungu chifukwa chani wakuchotserani mtendere. **KUTSATIRA** ndi kuvomereza molapa, ndipo chotsatira chake ndi kukhululukidwa komanso mtendere wa Mulungu **komanso** kuyeretsedwa kuti mukhale ndi mphamvu yokana tchimo.

kupitiriza kuchimwa. Kulapa ndikubwera pamaso pa Mulungu ndi mtima wosweka ndikunena kuti, “Ambuye, ndachimwira inu. Ndikudziwa kuti ndikuyenera kupita ku Gehena. Chonde, mundikhululukire ndi kundiyeretsa ku tchimoli pakuti sindikufuna kupitilira kukhala mu uchimo”. Mukuyenera kukhala ndi malingariro owona pamene mukulapa. (2 Akorinto 7:10) Ngati mtima wanu siuli woongoka, simukhululukidwa komanso simupatsidwa mphamvu yokana tchimo. Pa Masalimo 51:17, Davide anaonetsa mtima owona ku tchimo lake pamene akunena kuti, “Nsembe za Mulungu ndizo mzimu wosweka, inu Mulungu, simudzaupeputsa mtima wosweka ndi wolapa”. Davide anasweka mtima ku tchimo lake, ifenso tikuyenera kutero popeza Mulungu amadana ndi tchimo.

Choncho, **KUMVETSERA** ndi kuzindikira kuti mwasowa mtendere, ndikumufunsa Mulungu chifukwa chani wakuchotserani mtendere. **KUTSATIRA** ndi kuvomereza molapa, ndipo chotsatira chake ndi kukhululukidwa komanso mtendere wa Mulungu **komanso** kuyeretsedwa kuti mukhale ndi mphamvu yokana tchimo.

mbukhuli sizikutanthauza kukhala moyo wopanda tchimo, popeza nthawi ndi nthawi timapezeka kuti tachimwa. Chomwe tikutanthauza ndikusakhala ndi chikhalidwe cha moyo wa uchimo. Zinthu monga kunama, kuba, kudana ndi anzathu, kusilira, zisakhale gawo la moyo wathu. Tikhoza kuvutika ndi tchimo m'moyo wathu; kuvutikako zikutanthauza kuti tili ndi mtima wofuna kulapa. Mulungu akhoza kukhululukira tchimo liri lonse koma pamene tikana kulapa, ndikupitiriza moyo wa uchimo, tikhoza kutaya chipulumutso chathu. (Aheberi 10:26-30). 1 Yohane 1:9 akuti: “Ngati tivomereza machimo athu ali wokhulupirika ndi wolungama Iye kuti atikhululukire machimo athu ndikutisambitsa kutichotsera chisalungamo chiri chonse”. Mawu ofunika pa vesili ndi “ngati”. Choncho kuti tilandire chikhululukiro tikuyenera kulapa pamene tachimwa. Kuipa kwa kusalapa, tikuona mu mavesi otsatirawa, omwe ndi chenjezo kwa a khristu.

Aroma 8:12-14 akutichenjeza kuti: “Chifukwa chake abale, ife tiri amangawa, si ache a thupi ayi ... ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa, koma ngati ndi Mzimu mufetsa zochita

mbukhuli sizikutanthauza kukhala moyo wopanda tchimo, popeza nthawi ndi nthawi timapezeka kuti tachimwa. Chomwe tikutanthauza ndikusakhala ndi chikhalidwe cha moyo wa uchimo. Zinthu monga kunama, kuba, kudana ndi anzathu, kusilira, zisakhale gawo la moyo wathu. Tikhoza kuvutika ndi tchimo m'moyo wathu; kuvutikako zikutanthauza kuti tili ndi mtima wofuna kulapa. Mulungu akhoza kukhululukira tchimo liri lonse koma pamene tikana kulapa, ndikupitiriza moyo wa uchimo, tikhoza kutaya chipulumutso chathu. (Aheberi 10:26-30). 1 Yohane 1:9 akuti: “Ngati tivomereza machimo athu ali wokhulupirika ndi wolungama Iye kuti atikhululukire machimo athu ndikutisambitsa kutichotsera chisalungamo chiri chonse”. Mawu ofunika pa vesili ndi “ngati”. Choncho kuti tilandire chikhululukiro tikuyenera kulapa pamene tachimwa. Kuipa kwa kusalapa, tikuona mu mavesi otsatirawa, omwe ndi chenjezo kwa a khristu.

Aroma 8:12-14 akutichenjeza kuti: “Chifukwa chake abale, ife tiri amangawa, si ache a thupi ayi ... ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa, koma ngati ndi Mzimu mufetsa zochita

Woyera ndipo amakhala ndi mtendere ndi Mulungu chifukwa **Aroma 8:6b** akuti “*chisamaliro cha Mzimu chiri moyo ndi mtendere*”. Mukawerenga pa **Akolose 3:1-17** akuti: “*fetsani uchimo uli onse ndipo “valani chikondi” ndipo pochita izi, mtendere wa Khristu uzalamulira mitima yathu*”.

Chikondi, kukhulupirika, chilungamo ndi mtendere zimayendera limodzi ndipo zimakumana ndi kupsopsonana monga **Masalimo 85:10** akunenera,

*“Chikondi ndi choonadi zikomanizana,
Chilungamo ndi mtendere zipsopsonana”.*

Yesaya 26:3 akukokomezeka za mtendere pamene akuti: “*Inu mudzasunga mtima wokhazikika mu mtendere weniweni, chifukwa ukukhulupirirani inu*”. Choncho pamene timvera ndi kutsatira liwu la Yesu, tizadziwa mtendere weni weni wa Mulungu.

CHINGACHITIKE NDI CHANI PAMENE TIMVERA NDI KUTSATIRA YESU?

Choyamba, zomwe ndakhala ndikulankhula

Woyera ndipo amakhala ndi mtendere ndi Mulungu chifukwa **Aroma 8:6b** akuti “*chisamaliro cha Mzimu chiri moyo ndi mtendere*”. Mukawerenga pa **Akolose 3:1-17** akuti: “*fetsani uchimo uli onse ndipo “valani chikondi” ndipo pochita izi, mtendere wa Khristu uzalamulira mitima yathu*”.

Chikondi, kukhulupirika, chilungamo ndi mtendere zimayendera limodzi ndipo zimakumana ndi kupsopsonana monga **Masalimo 85:10** akunenera,

*“Chikondi ndi choonadi zikomanizana,
Chilungamo ndi mtendere zipsopsonana”.*

Yesaya 26:3 akukokomezeka za mtendere pamene akuti: “*Inu mudzasunga mtima wokhazikika mu mtendere weniweni, chifukwa ukukhulupirirani inu*”. Choncho pamene timvera ndi kutsatira liwu la Yesu, tizadziwa mtendere weni weni wa Mulungu.

CHINGACHITIKE NDI CHANI PAMENE TIMVERA NDI KUTSATIRA YESU?

Choyamba, zomwe ndakhala ndikulankhula

Mwina sizingakhale zoonza kunena kuti pamene tasowa mtendere, pali vuto pakati pa ife ndi Mulungu. Komanso mukaonetsetsa, izi zikhoza kukhala zoonza. Zovuta za m’banja, chuma, ntchito komanso thanzi ziriponseponse koma pa **Mateyu 11:28-29** Yesu akuti: “*Idzani kwa Ine, inu nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; chifukwa ndiri wofatsa ndi wodzichepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu.*” Mpumulo umenewu ndiye mtendere wa Mulungu. Komanso, ambiri aife tikuyenera kulapa pokakamira kukhala oyamba chifukwa **Afilipi 2:3** akuti tisapenyere za ife eni, koma tikhale akapolo, monga Khristu Yesu anachita. Pali akhristu ambiri amene amakhala ndi mkwiyo pamene akhala pambuyo pa anzawo ndipo amang’ung’udza kapena kunena miseche. Tikuyenera kulapa kuzinthu zonsezi komanso kusakonda konse komwe tili nako.

NTCHITO YA MZIMU WOYERA

Ndikofunikira kumvetsetsa kuti siungagonjetse tchimo ndi mphamvu yako, koma ndi Mulungu, zonse ndizotheka. Ndilonjezo la Mulungu kuti, kudzera mwa Mzimu Woyera, mungathe

Mwina sizingakhale zoonza kunena kuti pamene tasowa mtendere, pali vuto pakati pa ife ndi Mulungu. Komanso mukaonetsetsa, izi zikhoza kukhala zoonza. Zovuta za m’banja, chuma, ntchito komanso thanzi ziriponseponse koma pa **Mateyu 11:28-29** Yesu akuti: “*Idzani kwa Ine, inu nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; chifukwa ndiri wofatsa ndi wodzichepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu.*” Mpumulo umenewu ndiye mtendere wa Mulungu. Komanso, ambiri aife tikuyenera kulapa pokakamira kukhala oyamba chifukwa **Afilipi 2:3** akuti tisapenyere za ife eni, koma tikhale akapolo, monga Khristu Yesu anachita. Pali akhristu ambiri amene amakhala ndi mkwiyo pamene akhala pambuyo pa anzawo ndipo amang’ung’udza kapena kunena miseche. Tikuyenera kulapa kuzinthu zonsezi komanso kusakonda konse komwe tili nako.

NTCHITO YA MZIMU WOYERA

Ndikofunikira kumvetsetsa kuti siungagonjetse tchimo ndi mphamvu yako, koma ndi Mulungu, zonse ndizotheka. Ndilonjezo la Mulungu kuti, kudzera mwa Mzimu Woyera, mungathe

kuyeretsedwa ku tchimo liri lonse. Palibe tchimo lalikulu pamaso pa Mulungu. **Aroma 8:4** akuti tiri ndi Mzimu “*kuti coikika chake cha chilamulo chikakwaniridwe mwa ife, amene sitiwendayenda monga mwa thupi, koma monga mwa Mzimu*”. Vesili likuti ngati tiwendayenda monga mwa Mzimu, tingakwaniritse KWATHUNTHU chilungamo chake cha Mulungu. Kumbukirani, pa **Masalimo 51:17**, Davide amalapa pokhala wachiwerewere, wonama, komanso wakupha koma Mulungu anamukhululukira chifukwa anasweka mtima ku tchimo lakelo.

Zokhudza ntchito za Mzimu, **Afilipi 2:13** akuti: “*pakuti wakuchita mwainu kufuna ndi kuchita komwe, chifukwa cha kukoma mtima kwake, ndiye Mulungu* [kudzera mwa Mzimu]”. Ndipo cholinga chake ndi kukusinthani inu pokupatsani mphamvu yokana tchimo kuti mukakhale moyo watsopano. Kudzera mwa Mzimu, munabadwa mwatsopano ndikupatsidwa mphamvu yosiya moyo wanu wauchimo wakale monga m'mene **2 Akorinto 5:17** akunenera, “*ngati munthu aliyense ali mwa Khristu, ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano!*”

kuyeretsedwa ku tchimo liri lonse. Palibe tchimo lalikulu pamaso pa Mulungu. **Aroma 8:4** akuti tiri ndi Mzimu “*kuti coikika chake cha chilamulo chikakwaniridwe mwa ife, amene sitiwendayenda monga mwa thupi, koma monga mwa Mzimu*”. Vesili likuti ngati tiwendayenda monga mwa Mzimu, tingakwaniritse KWATHUNTHU chilungamo chake cha Mulungu. Kumbukirani, pa **Masalimo 51:17**, Davide amalapa pokhala wachiwerewere, wonama, komanso wakupha koma Mulungu anamukhululukira chifukwa anasweka mtima ku tchimo lakelo.

Zokhudza ntchito za Mzimu, **Afilipi 2:13** akuti: “*pakuti wakuchita mwainu kufuna ndi kuchita komwe, chifukwa cha kukoma mtima kwake, ndiye Mulungu* [kudzera mwa Mzimu]”. Ndipo cholinga chake ndi kukusinthani inu pokupatsani mphamvu yokana tchimo kuti mukakhale moyo watsopano. Kudzera mwa Mzimu, munabadwa mwatsopano ndikupatsidwa mphamvu yosiya moyo wanu wauchimo wakale monga m'mene **2 Akorinto 5:17** akunenera, “*ngati munthu aliyense ali mwa Khristu, ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano!*”

tikuchita nkhaza kwa amuna athu, akazi athu, kapena abale athu, ndife achinyengo. Pa **Aefeso 5:25** tikuzidwa kuti “*Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Khristu anakonda Ekelesia, nadzipereka yekha m'malo mwake.*”

NJIRA YA MTENDERE

Kawirinso, KUMVETSERERA ndikuzindikira kuti mwasowa mtendere, ndikumufunsa Mulungu chifukwa chani wachotsa mtendere wanu. KUTSATIRA ndikuvomereza kwa Mulungu molapa, ndipo chotsatira chimakhala kukhululukidwa ndi mtendere pakati pa inu ndi Mulungu, komanso mphamvu yokana tchimo lamtsogolo.

Pamene tachimwa, mtendere wathu ndi Mulungu umasowa.

Pamene talapa, mtendere wathu umabwerera Nthawi iri yonse tikasowa mtendere, pali vuto pakati pa ife ndi Mulungu.

Aroma 8:14 akuti: “*Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo, ali ana a Mulungu*”. Choncho ana a Mulungu amamvera ndi kutsatira chitsogozo cha Mzimu

tikuchita nkhaza kwa amuna athu, akazi athu, kapena abale athu, ndife achinyengo. Pa **Aefeso 5:25** tikuzidwa kuti “*Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Khristu anakonda Ekelesia, nadzipereka yekha m'malo mwake.*”

NJIRA YA MTENDERE

Kawirinso, KUMVETSERERA ndikuzindikira kuti mwasowa mtendere, ndikumufunsa Mulungu chifukwa chani wachotsa mtendere wanu. KUTSATIRA ndikuvomereza kwa Mulungu molapa, ndipo chotsatira chimakhala kukhululukidwa ndi mtendere pakati pa inu ndi Mulungu, komanso mphamvu yokana tchimo lamtsogolo.

Pamene tachimwa, mtendere wathu ndi Mulungu umasowa.

Pamene talapa, mtendere wathu umabwerera Nthawi iri yonse tikasowa mtendere, pali vuto pakati pa ife ndi Mulungu.

Aroma 8:14 akuti: “*Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo, ali ana a Mulungu*”. Choncho ana a Mulungu amamvera ndi kutsatira chitsogozo cha Mzimu

Ndinali wamanyazi kulankhula kunthawi yophunzitsana mawu a Mulungu ndipo ndimalephera kupita ku misonkhano ya mapemphero chifukwa mutu unali kundipweteka kwambiri. Sindimapeza bwino kukhala pa gulu la wanthu komanso kulankhula Uthenga Wabwino. Tsiku lina ndinagwada pansi, ndimisonzi, ndipo ndinati, “Akhristu akuyenera kukhala moyo wachigonjetso, koma ine ndine wamantha komanso wogonjetsedwa. Ngati mukufuna kuti ndisinthe, mundisinthe Ambuye.” Sindinaona kusintha kuli konse nthawi yomweyo koma m’wawa wake ndinakomana ndi m’bale wina yemwe anali kulalikirira pa njira. Atamaliza kulalikirira, anandiuza kuti nanenso ndilalikirira. Ndinaima, Baibulo liri m’dzanja langa, ndipo ndinalalikirira molimba mtima komanso mtima wanga uli pansi. Iyitu inali mphamvu ya Mzimu Woyera. Ndinamasulidwa ndipo **Yohane 8:36** akuti: “*ngati Mwana adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu*”.

Mwina malo oyenera kuti tilumikizane bwino ndi Mulungu ndi panyumba pathu. Chiyero chimayambira m’banja mwathu. Ngati tili achikondi komanso achifundo ndi anzathu, koma

Ndinali wamanyazi kulankhula kunthawi yophunzitsana mawu a Mulungu ndipo ndimalephera kupita ku misonkhano ya mapemphero chifukwa mutu unali kundipweteka kwambiri. Sindimapeza bwino kukhala pa gulu la wanthu komanso kulankhula Uthenga Wabwino. Tsiku lina ndinagwada pansi, ndimisonzi, ndipo ndinati, “Akhristu akuyenera kukhala moyo wachigonjetso, koma ine ndine wamantha komanso wogonjetsedwa. Ngati mukufuna kuti ndisinthe, mundisinthe Ambuye.” Sindinaona kusintha kuli konse nthawi yomweyo koma m’wawa wake ndinakomana ndi m’bale wina yemwe anali kulalikirira pa njira. Atamaliza kulalikirira, anandiuza kuti nanenso ndilalikirira. Ndinaima, Baibulo liri m’dzanja langa, ndipo ndinalalikirira molimba mtima komanso mtima wanga uli pansi. Iyitu inali mphamvu ya Mzimu Woyera. Ndinamasulidwa ndipo **Yohane 8:36** akuti: “*ngati Mwana adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu*”.

Mwina malo oyenera kuti tilumikizane bwino ndi Mulungu ndi panyumba pathu. Chiyero chimayambira m’banja mwathu. Ngati tili achikondi komanso achifundo ndi anzathu, koma

Mzimu Woyera amatipatsa mphamvu zokhala moyo wa umulungu. **2 Petro 1:3-4** akuti, “*Popeza mphamvu ya umulungu wache idatipatsa ife zonse za pamoyo ndi chipembedzo ... kuti MUTAPULUMUKA KUCHIVUNDI chiri pa dziko lapansi m’chilakolako*”. **Tito 2:11-12** akuvomerezana ndi mawuwa, “*Pakuti chaonekera chisomo cha Mulungu chakupulumutsa anthu onse, ndi kutiphunzitsa ife kuti pokana chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m’dziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedza*”.

Choncho, tikuona pamavesi amenewa kuti Mulungu amapereka Mzimu Woyera kuti tiziletse ku tchimo, komanso tisakhale akapolo ku tchimo, koma kukhala ndi mphamvu ya umulungu kukhala moyo wodziletsa, woyera komanso wokondweretsa Mulungu (**Aroma 12:1-2**).

ZITSANZO ZOCHITIKA PA MOYO WANGA

Ndikufuna tsopano kupereka zitsanzo za momwe Mulungu anasinthila moyo wanga.

Panali mzimayi wina yemwe zimandivuta kuti

Mzimu Woyera amatipatsa mphamvu zokhala moyo wa umulungu. **2 Petro 1:3-4** akuti, “*Popeza mphamvu ya umulungu wache idatipatsa ife zonse za pamoyo ndi chipembedzo ... kuti MUTAPULUMUKA KUCHIVUNDI chiri pa dziko lapansi m’chilakolako*”. **Tito 2:11-12** akuvomerezana ndi mawuwa, “*Pakuti chaonekera chisomo cha Mulungu chakupulumutsa anthu onse, ndi kutiphunzitsa ife kuti pokana chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m’dziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedza*”.

Choncho, tikuona pamavesi amenewa kuti Mulungu amapereka Mzimu Woyera kuti tiziletse ku tchimo, komanso tisakhale akapolo ku tchimo, koma kukhala ndi mphamvu ya umulungu kukhala moyo wodziletsa, woyera komanso wokondweretsa Mulungu (**Aroma 12:1-2**).

ZITSANZO ZOCHITIKA PA MOYO WANGA

Ndikufuna tsopano kupereka zitsanzo za momwe Mulungu anasinthila moyo wanga.

Panali mzimayi wina yemwe zimandivuta kuti

ndimukonde. Ndimamuthawa, osalankhulana naye, koma tsiku lina ndinasowa mtendere pamene Ambuye ananditsutsa ku tchimo ili ndipo ndinati, "Ambuye, ndizolakwika kuti sindimukonda mlongo wanga. Chonde, ndithandizeni kumukonda." Zitatha izi, ndinapita kukaonana naye ndipo pamene ndinayamba kulankhula naye, Ambuye anasinth mtima wanga. Zodabwitsa ndizakuti, tinakhala pachimzake chenicheni ndipo ndinali ndi mtendere ndi iye komanso ndi Mulungu. Sindinayenera kudabwa chifukwa Mulungu angathe kupanga chiri chonse, koma zinali zazikulu kwa ine kuti Mulungu anandiyeretse ku tchimo ili komanso kusintha moyo wanga wosakonda ndi mtima wanga wouma.

Pa **Yohane 13:34**, Mulungu akutilamula kukondana wina ndi mzake. Kodi pali wina woti mukuyenera kuyanjana naye? Tikuuzidwa kuti tikondane nawo adani athu. Ngati ukudana ndi munthu wina, ukuyenera kulapa. Pa **Aroma 12:18** akuti, "*Ngati nkutheka monga momwe mukhoza, khalani ndi mtendere ndi anthu onse*". Tizitha kumuyang'ana mzathu m'maso komanso "*kukondana kuchokera pansu pa mtima*" (**1 Petro**

ndimukonde. Ndimamuthawa, osalankhulana naye, koma tsiku lina ndinasowa mtendere pamene Ambuye ananditsutsa ku tchimo ili ndipo ndinati, "Ambuye, ndizolakwika kuti sindimukonda mlongo wanga. Chonde, ndithandizeni kumukonda." Zitatha izi, ndinapita kukaonana naye ndipo pamene ndinayamba kulankhula naye, Ambuye anasinth mtima wanga. Zodabwitsa ndizakuti, tinakhala pachimzake chenicheni ndipo ndinali ndi mtendere ndi iye komanso ndi Mulungu. Sindinayenera kudabwa chifukwa Mulungu angathe kupanga chiri chonse, koma zinali zazikulu kwa ine kuti Mulungu anandiyeretse ku tchimo ili komanso kusintha moyo wanga wosakonda ndi mtima wanga wouma.

Pa **Yohane 13:34**, Mulungu akutilamula kukondana wina ndi mzake. Kodi pali wina woti mukuyenera kuyanjana naye? Tikuuzidwa kuti tikondane nawo adani athu. Ngati ukudana ndi munthu wina, ukuyenera kulapa. Pa **Aroma 12:18** akuti, "*Ngati nkutheka monga momwe mukhoza, khalani ndi mtendere ndi anthu onse*". Tizitha kumuyang'ana mzathu m'maso komanso "*kukondana kuchokera pansu pa mtima*" (**1 Petro**

1:22b). Kukondana wina ndi mzake si chithu chongokhala bwino kuchita ayi, koma ndilamulo lomwe likubwera ndi chenjezo. Pa **1 Yohane 4:20; 3:15** tikuuzidwa kuti, "*Munhtu akati kuti ndikonda Mulungu, nadana naye m'bale wake, ali wabodza; pakuti iye wosakonda mbale wake amene amuwona, sakhoza kukonda Mulungu amene samuona ... Yense wakudana ndi mbale wace ali wakupha munthu, ndipo mudziwa kuti wakupha munthu ali yense, alibe moyo wosatha wakukhala mwa iye.*"

Ntchito ya Mulungu yakuyeretse, ingafanizidwe ndi ntchito ya munthu wokonza magalimoto. Timamufunsa makaniki kuti akonze galimoto yathu, Abale, Yesu ndi mlengi wathu ndipo tikamufunsa Iye kuti agwire ntchito mwa ife, atisinth ndipo tikhala moyo wokondweretsa Iyeyo. Yesu satikakamiza kuchita izi. Ndipamene tiri ofuna kumvera ndi kutsatira liwu lake, azatiyeretse ndikusintha mitima yathu.

Ambuye anandiwombola ku mizimu yoledzera, kutukwana, kunama, kuba ndi machimo ena woti sindingawatchule, koma kundipulumutsa ku manyazi chinali cha mtengo wapatali kwa ine.

1:22b). Kukondana wina ndi mzake si chithu chongokhala bwino kuchita ayi, koma ndilamulo lomwe likubwera ndi chenjezo. Pa **1 Yohane 4:20; 3:15** tikuuzidwa kuti, "*Munhtu akati kuti ndikonda Mulungu, nadana naye m'bale wake, ali wabodza; pakuti iye wosakonda mbale wake amene amuwona, sakhoza kukonda Mulungu amene samuona ... Yense wakudana ndi mbale wace ali wakupha munthu, ndipo mudziwa kuti wakupha munthu ali yense, alibe moyo wosatha wakukhala mwa iye.*"

Ntchito ya Mulungu yakuyeretse, ingafanizidwe ndi ntchito ya munthu wokonza magalimoto. Timamufunsa makaniki kuti akonze galimoto yathu, Abale, Yesu ndi mlengi wathu ndipo tikamufunsa Iye kuti agwire ntchito mwa ife, atisinth ndipo tikhala moyo wokondweretsa Iyeyo. Yesu satikakamiza kuchita izi. Ndipamene tiri ofuna kumvera ndi kutsatira liwu lake, azatiyeretse ndikusintha mitima yathu.

Ambuye anandiwombola ku mizimu yoledzera, kutukwana, kunama, kuba ndi machimo ena woti sindingawatchule, koma kundipulumutsa ku manyazi chinali cha mtengo wapatali kwa ine.